# Mabanja acikristu

## Maphunziro a anthu opezeka m'ukwati ndi a makolo

1. Maziko a ukwati wacikristu
2. Ukwati wacikristu
3. Azimuna acikristu
4. Azimai acikristu
5. Makolo acikristu monga zitsanzo
6. Makolo acikristu monga aziphunzitsi
7. Mabanja acikristu

## Malangizo a mphunzitsi

- Mfundo zimene zidzakambidwapo zingawawe aphunzi ena (mwacitsanzo cifukwa ca kukumbukira ukwati woipa wa makolo kapena cifukwa ca kuthetsedwa kwa ukwati wa iwo eni kapena cifukwa mwamuna/mkazi wao sawacitira zabwino kapena cifukwa ca kusowa mwana). Khalani ozindikira za izi pa kusankha mau anu, koma osasintha zoonadi za m'Baibulo.
- Khalani ozindikira kuti aphunzi ena adzayamba kumvetsa kuti anacimwa (mwacitsanzo cigololo, kulephera pa kukhala mwamuna/mkazi wabwino kapena kholo labwino, kugonana asanakwatirane). Osawalola kupita kunyumba asamvera bwino pa zimene anacita, koma auzeni kulapa ndi kuika ciyembekezo cao mwa Yesu Kristu Mpulumutsi.
- Colinga ca maphunziro ndi kuti aphunzi amvetsa kuti:
  - Colinga cacikulu coposa ca miyoyo yathu ndico kumvera ndi kukondweretsa Mulungu.
  - Ukwati ndi cinthu colemekezeka ndi Mulungu ndipo cifukwa cace ifenso tiyenera kulemekeza ukwati.
  - Tiyenera kutenga ulamuliro pa ukwati wathu ndi pa ana athu.
- Maphunziro awa atiphunzitsa za ukwati wacikristu¸ makolo acikristu ndi mabanja acikristu. Kopanda Yesu kukhala Mpulumutsi wathu, sitingakhale m'ukwati wacikristu kapena kukhala makolo acikristu kapena mabanja acikristu. Cifukwa cace, tsimikizirani m'phunziro lirilonse cofunikira ca kuyanjanitsidwa ndi Mulungu mwa Yesu Kristu. Sitingakhale miyoyo yathu m'njira momwe Mulungu afuna koma cabe ngati tayanjanitsidwa ndi Mulungu. Sitingakhale ndi ukwati wabwino, sitingakhale makolo okondwera kapena mabanja osangalala koma cabe ngati tayanjanitsidwa ndi Mulungu. Kuyanjanitisdwa ndi Mulungu ndiko mphatso wodabwitsa wa Mulungu womwe sitiyenera kulandira. Ndiwo mphatso wodabwitsa koposa womwe tingalandire, ndiye kambiranani mphatso mwaulemu, modzicepetsa ndi moyamikira.

*Komatu khala citsanzo kwa iwo okhulupira, m'mau, m'mayendedwe, m'cikondi, m'cikhulupiriro, m'kuyera mtima – 1 Timoteo 4.12b*

## Phunziro 1 Maziko a ukwati wacikristu

<u>Zofunikira pa nthawi ya kuphunzira</u>
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

## 1. Kulandiridwa (10 minutes)
- Landirani onse.
- Fotokozani kuti maphunziro awa adzaphunzitsa anthu opezeka m'ukwati ndi makolo za kukhala banja labwino pa maso pa Mulungu.
- M'phunziro lirilonse tidzawerenga Baibulo, pakuti maphunziro onse amangidwa pa zimene Baibulo liphunzitsa.

<u>Zidziwitso</u>
- Maphunziro awa ndi a azimuna ndi azimai amene apezeka m'ukwati, a iwo amene anakwatiwapo ndiponso a iwo amene ali ndi mwana koma sapezeka m'ukwati.
- Phunziro lirilonse lidzayamba pa nthawi ya …………. koloko. Fikani pa nthawi yake cifukwa ngati ticedwa, sitidzakhala ndi nthawi yokwanira.
- Ndi cofunikira kwambiri kubwera ku maphunziro onse.
- Aphunzi ayenera kubwera ndi Baibulo ku maphunziro onse. Tilifuna pa nthawi ya kuphunzira.
- M'phunziro lotsiriza tidzalemba mayeso (mphunzitsi adzasankha ngati mayeso adzalembedwa). Kulemba mayeso sikudzakhala bvuto ngati mudzaphunzirako maphunziro onse.

<u>Malamulo</u>
- Ana sadzaloledwa pa nthawi ya maphunziro (makanda adzaloledwa ngati sasokoneza aphunzi).
- Osayenda-yenda pa nthawi ya kuphunzira.
- Khalani bwino ndipo mverani bwino aphunzitsi anu. Khalani omasuka.

- Funsani aphunzi ngati ali ndi mafunso.
- Pemphani Mulungu dalitso pa phunziro iri.

## 2. Citanthauzo ca ukwati (20 minutes)
- Funsani aphunzi citanthauzo ca ukwati: kodi ukwati ndi ciani?
  Yankho: ukwati ndi
  - <u>Ubale</u> m'mene mwamuna ndi mkazi abwera pamodzi ndipo agonana.
  - <u>Ciyanjano</u> ca mwamuna ndi mkazi: akhala amodzi, osati za m'thupi cabe, komanso za m'zokhudza ndi za m'uzimu.
  - <u>Cipangano</u> (Malaki 2.14) ca pa maso pa Mulungu cimene siciyenera kuphwanyedwa: ukwati suyenera kuthetsedwa. Cifukwa ca ici, kudzipereka ndi kofunikira kwambiri: khalani okhulupirika, osathawa pa nthawi ya mabvuto. Si cipangano ca pa maso pa Mulungu cabe komanso ca pa maso pa boma lathu. Cifukwa cace tiyenera kukwatira/kukwatiwa monga mwa malamulo a dziko limene tikhalamo.
- Funsani aphunzi za ciyambi ca ukwati: kodi ganizo la kukwatira/kukwatiwa licokera kuti?
  Yankho: Kwa Mulungu Mlengi amene anauza anthu oyamba Adamu ndi Hava kukhala amodzi. Ndiye ukwati wao unayambitsidwa ndi Mulungu.

## 3. Ukwati woyamba (20 minutes)
- Werengani pamodzi <u>Genesis 2.18-25</u>.

- Lembani mafunso awa pa bolodi ndipo lolani aphunzi kuwayankha m'magulu ang'ono. Kapena yankhani mafunso pamodzi.

**Mafunso**
1. Ndi yani amene anafuna kuti Adamu akwatire, kulingana ndi ndime ya 18?
2. Cifukwa ciani Mulungu analenga mkazi? M'ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi Mulungu analenga bwanji Hava? M'ndime iti mwapeza yankho?
4. Cifukwa ciani Mulungu anagwiritsa nchito nthiti ya Adamu, kulingana ndi inu?
5. Kodi ukwati wa Adamu ndi Hava unali wabwino kapena woipa?
6. Kodi Mulungu atipatsa langizo lotani m'ndime ya 24?

- Mayankho abwino ali conco:
  1. **Ndi yani amene anafuna kuti Adamu akwatire, kulingana ndi ndime ya 18?**
     Yankho: Mulungu. Ici citanthauza kuti ukwati ndi mphatso wa Mulungu.
  2. **Cifukwa ciani Mulungu analenga mkazi? M'ndime iti mwapeza yankho?**
     Yankho: Pakuti kunali kwabwino kuti Adamu akhala ndi munthu wina pafupi naye womthandiza. Ndime ya 18.
  3. **Kodi Mulungu analenga bwanji Hava? M'ndime iti mwapeza yankho?**
     Yankho: Anagwiritsa nchito nthiti ya Adamu kupanga Hava. Ndime ya 21.
  4. **Cifukwa ciani Mulungu anagwiritsa nchito nthiti ya Adamu, kulingana ndi inu?**
     Yankho: Baibulo sitiuza cifukwa cace, koma anthu ena aganiza kuti Mulungu anasankha nthiti cifukwa nthiti zikhala pafupi ndi mtima (cikondi, ciyanjano, ubwenzi, kufanana).
  5. **Kodi ukwati wa Adamu ndi Hava unali wabwino kapena woipa?**
     Yankho: Iwo anakhala ndi ukwati wabwino. Adamu anakondwera ndi mphatso ya Mulungu. Kunalibe manyazi kapena mantha, koma cikondwerero, cikondi ndi ciyanjano.
  6. **Kodi Mulungu atipatsa langizo lotani m'ndime ya 24?**
     Yankho: Anthu amene afuna kukwatira/kukwatiwa, ayenera:
     1. Kusiya makolo ao
        Ici citanthauza kusiya m'njira ziwiri: m'thupi (kusamuka) komanso m'mtima (kusadalirabe pa makolo, kuthetsa mabvuto a iye mwini). Makolo angapangire ana ao opezeka m'ukwati, koma alibe mphamvu m'njira ina iriyonse.
     2. Kudziphatikana (kukwatirana). Ici citanthauza kukhala amodzi.
     3. Kukhala thupi limodzi (kugonana). Ici ndi cizindikiro ca ciyanjano ndiponso cinthu cotsiriza ca kulakalaka ciyanjano ceniceni, osati cinthu coyamba!

     Ndi mwamuna amene afulumizitsa ukwati.

## 4. Ukwati wa masiku onse (10 minutes)
- Bwerezani kuti Adamu ndi Hava anali ndi ukwati wabwino.
- Fotokozani ndi cifukwa ciani anthu ambiri abvutika ndi mabvuto ambiri m'maukwati ao masiku ano.
  Yankho: Adamu ndi Hava sanamvere Mulungu: iwo anacimwa.
  Zonse zasinthika:
  - Ubale wa Mulungu ndi anthu watsira. Ndife otembereredwa ndi Mulungu cifukwa ca macimo athu. Tiyenera Yesu kutipulumutsa ku macimo athu ndi kukonza ubwenzi wa Mulungu ndi ife.
  - Ubale wa anthu watsira. Ici ndi cifukwa cace muli mabvuto ambiri m'maukwati. Mulungu afunabe maukwati kukhala abwino; tidzaphunzira zina za ici m'maphunziro otsatira. Tifunika Yesu kuti tiphunzire kukhala m'ubale wabwino ndi anthu ena.
  - Ubale wa anthu ndi cilengedwe watsira. Tsono tikumana ndi imfa, matenda, nyama zoopsya ndi zina zotere. Tifunika Yesu kuti tiphunzire kukhala m'ciyanjano ndi cilengedwe cace.
- Fotokozani kuti kuyanjananso ndi kotheka mwa Yesu cabe. Cifukwa cace ndi cofunikira kukhala olumikizidwa ndi Mulungu mwa Yesu, ngakhale m'ukwati.

## 5. Colinga ca ukwati (10 minutes)

- Funsani aphunzi za colinga ca ukwati:
  - Ciyanjano, thandizo, cikondwerero (Genesis 2.18).
  - Kupewa madama (1 Akorinto 7.2 ndi 9); kukhala oyera pa maso pa Mulungu.
  - Kucuruka (Genesis 1.28) kuti tikhale ndi ana oopa Mulungu amene amlemekeza (Malaki 2.15).
- Afunseni cofunikira ca kukhala m'ukwati ndi kukhala ndi ana.
  Fotokozani kuti:
  - Kukhala ndi ana ndi kofunikira kulingana ndi Baibulo. Komabe, pa dziko lathu lapansi pali mabvuto cifukwa ca chimo loyamba, ndiye anthu ena salandira mwana.
  - Colinga ca miyoyo yathu ndico kudziwa Mulungu ndi kumumvera (Deuteronomo 10.12 ndi 13, Mika 6.8). Kudziwa Mulungu ndi kumumvera ndi kofunikira koposa kukhala m'ukwati ndi kukhala ndi ana. Ukwati ndi cinthu cosakhazikika (ukwati utsira pamene mwamuna/mkazi amwalira), koma ciyanjano ca anthu ndi Mulungu sicitsira.
  - Mu Baibulo tiwerenga za anthu amene anakhala monga mwa colinga ca Mulungu, koma sanapezeke m'ukwati ndipo analibe mwana. Kulingana ndi 1 Akorinto 7.8, 9 ndi 34, palibe bvuto kusapezeka m'ukwati (ndiponso kusakhala ndi mwana).
  - Kusudzula ndi 'mayankho ena' siziloledwa pa nkhani iyi.

## 5. Kusankha mwamuna/mkazi (10 minutes)

- Funsani aphunzi kuti ndi ciani cimene ciri cofunikira m'mwamuna/mkazi wao watsogolo ndi wa ana ao.
  Yankho: Ndi cofunikira kwambiri kuti anthu adziwana asanalowe m'ukwati. Mwacitsanzo: Kodi akonda ciani, acita ciani pa kukakamizidwa ndi pa nthawi ya mabvuto (monga maliro), abvala ciani, acita ciani pa tsiku, asewenzetsa bwanji ndalama, aganiza ciani za Mulungu, mbiri yao ndi ciani, kufoka kwao ndi kotani? Kodi ali wokhulupirika? Kodi angakhale tate/mai wabwino ndipo ine (mkazi) ndifuna kudzipereka kwa iye kapena ine (mwamuna) ndifuna kuwatumikira kodi?
- Malizitsani pa kunena kuti ukwati suyenera kuthetsedwa, cifukwa cace osathamangirako. Akumbutseni kuti m'ukwati wacikristu, Kristu ndiye maziko ndipo cikondi, ulemu ndi cisamaliro ndizo zofunikira koposa.

## 6. Kutsiriza (5 minutes)

- Bwerezani mwacidule phunziro la lero: ukwati ndi mphatso ya Mulungu ndipo Iye ayenera kukhala maziko a ukwati.
- Pempherani.

## Phunziro 2 Ukwati wacikristu

<u>Zofunikira pa nthawi ya kuphunzira</u>
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

## 1. Kulandiridwa (5 minutes)
- Landirani aphunzi.
- Pempherani.
- Bwerezani mwacidule zimene zinakambidwira m'phunziro 1: ukwati ndi mphatso ya Mulungu ndipo Iye ayenera kukhala maziko ake.
- Dziwitsani mutu wa lero: tidzayang'anirapo zotsatira za pafupifupi za kudziwa kuti ukwati ndi mphatso ya Mulungu. Tidzayang'anira mfundo zimene ziri zofunikira za amuna ndi akazi. M'maphunziro ena a m'tsogolo tidzayang'angira kusiyana kwa udindo wa amuna ndi akazi.

## 2. Mabvuto a m'ukwati – zolowapo (40 minutes)
- Funsani aphunzi za mabvuto amene iwo anaona kapena amene anapeza m'ukwati. Lembani mayankho ao pa bolodi.
- Uzani aphunzi kukhala m'magulu ang'ono ndiponso gulu lirilonse kukamba za colowapo cimodzi.

**Zolowapo**

**1. Nelson ndi Victoria**

Nelson ndi Victoria anayamba ukwati wao mwezi watha. Victoria sakondwera. Masiku onse Nelson amamuuza, 'Ndinu mkazi woipa pakuti simudziwa kuphika bwino nsima. Ndilakalaka kuti ndinakwatira mbale wanu. Ngati simudzayamba kuphika bwino, ndidzakusiyani'. Victoria ayankha kuti adzayesadi. Akumva cisoni pakuti Nelson amudandaulira.

1. Kodi mudziwa anthu amene anathetsa ukwati?
2. Kodi Victoria ayenera kucita ciani?
3. Kodi Baibulo likamba ciani za kuthetsa ukwati?
4. Kodi Nelson ayenera kucita ciani?

**2. Bernard ndi Zelipa**

Bernard ndi Zelipa ndiwo okwatirana zaka zitatu. Ali ndi mwana m'modzi. Bernard amakonda mkazi wake ndipo ayesa kumsangalatsa. Anapeza nchito ndipo amagwiritsa nchito ndalama zimene iye apeza kuthandiza banja lake. koma angakhale ayesa zonse, Zelipa amauza anzake nkhani zoipa za iye.

1. Kodi mudziwa anthu amene amauza anthu ena za mabvuto a m'ukwati?
2. Kodi Bernard akumva bwanji za mkazi wake, kulingana ndi inu?
3. Kodi Bernard ayenera kucita ciani?

**3. Cisomo ndi Rakele**

Cisomo amakonda Rakele. Iwo si ndiwo okwatirana, koma anagonana kangapo. Cisomo sakhala wotsimikiza ngati afuna kukwatira Rakele kapena iai. Tsiku lina Rakele azindikira kuti ali ndi mimba.

1. Kodi mudziwa anthu amene anagonana iwo asanakwatirane?
2. Kodi Baibulo linena ciani za kugonana kunja kwa ukwati?
3. Kodi mungapangire Cisomo ndi Rakele kucita ciani?

**4. Lemekani ndi Sara**

Lemekani ndi Sara apezeka m'ukwati zaka zitatu. Alibe mwana. Lemekani aika mlandu pa Sara posabereka mwana. Cifukwa ca ici, iwo amalimbana. Usiku uliwonse Lemekani anena, 'Usiku uwu

muyenera kugona ndi ine. Ndifuna mwana'. Lemekani afuna iwo kugwiritsa nchito mankhwala a ufiti kuti angakhale ndi mwana. Sara akana. Lemekani akamba kuti adzamusiya ndipo Sara adzafa ali yekha kopanda mwana.

1. Fotokozani cofunikira ca kukhala ndi mwana.
2. Kodi zifukwa zake za kukhala kopanda mwana ndizo ciani?
3. Kodi mungapangire Lemekani ndi Sara kucita ciani?

**5. Richard ndi Edina**

Richard ndi Edina ndiwo okwatirana zaka zisanu. Richard ali ndi nchito. Amagwira nchito molimba kukhala ndi ndalama zambiri. Afuna kuonetsa anthu okhala pafupi naye kuti iye ndi munthu wabwino ndi wakugwira nchito kwambiri. Afuna kulemera ndi kugula galimoto. Cifukwa cake safuna kugula ciriconse cimene banja lisowa koma cabe cakudya ndi zobvala zocepa. Edina sakondwera cifukwa ca ico. Iye aganiza kuti Richard ayenera kugula zonse zimene banja lifunika ndiponso kuti sayenera kukhala aumbombo. Richard amayankha kuti Edina saloledwa kunena ciriconse ca ndalama, pakuti iye yemwe ndi mwini wa ndalama iye akhoza kucita cimene afuna.

1. Fotokozani cifukwa ciani Richard ndi Edina amakambirana zambiri za ndalama.
2. Kodi Baibulo litiuza ciani za kusewenzetsa ndalama?
3. Kodi mungapangire Richard ndi Edina kucita ciani?

**6. Danieli ndi Dorothy**

Danieli ndi Dorothy ali ndi ana asanu ndi awiri. Amakhala m'mudzi ndipo kumeneko Danieli sakhoza kupeza ndalama. Cifukwa cake, Danieli afuna kusiya banja lake ndi kukhala ku Lusaka. Alonjeza kuwatumira ndalama kuti banja likhale ndi moyo. Dorothy akondwera kuti Danieli adzakwaniritsa kuthandiza banja. Koma sakondwera kuti mwamuna wake adzakhala kutali nthawi yaitali. Akumva kuti kukhala banja labwino kudzakhala kobvuta ngati tate ali kutali.

1. Kodi mudziwa anthu amene sakhala pamodzi iwo angakhale ndiwo okwatirana?
2. Kodi mungapangire ciani Danieli ndi Dorothy?

**7. Amos ndi Selina**

Amos ndi Selina apezeka m'ukwati zaka ziwiri. Selina ali ndi pakati pa miyezi 7 ndi mwana wao woyamba. Amos afuna kugona naye. Koma Selina ayankha kuti sadzakwaniritsa cifukwa ca kukhala ndi pakati ndiponso kuti ayenera kuyembekeza miyezi ina mpaka aciritsidwa bwino atabala mwana. Amos akamba kuti sakhoza kuyembekeza kwambiri. Aganiza za kupeza mkazi wina mpaka Selina akadzakhala wokonzeka kugona naye.

1. Kodi mungapangire ciani Amos?

- Mayankho abwino ali conco:

  **Nelson ndi Victoria**

  1. **Kodi mudziwa anthu amene anathetsa ukwati?**
     Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.
  2. **Kodi Victoria ayenera kucita ciani?**
     Yankho: Ayenera kupempha Mulungu thandizo, ayenera kupitiriza kuyesa komanso kupempha upangiri kwa Akristu anzeru.
  3. **Kodi Baibulo likamba ciani za kuthetsa ukwati?**
     Yankho: Awerengereni Mateyu 19.3-6. Kuthetsa ukwati ndi kololeka cabe ngati m'modzi wa okwatirana acita cigololo (Mateyu 19.9). Kwa Akristu, kukhululukirana ndi kuyanjananso ndizo zabwino kuposa kusudzula. Ngati anthu asudzula, iwo saloledwa kukwatiranso/kukwatiwanso mpaka mwamuna/mkazi amwalira (1 Akorinto 7.11).
     Kwa mphunzitsi: osafotokozera zambiri, koma ngati aphunzi apempha kuphunzira zina zambiri zimene Baibulo liphunzitsa pa nkhani ya kuthetsa ukwati, auzeni Mau a Mulungu ocokera m'Aroma 7.1-3, Marko 10.12 ndi Luka 16.18.

4. **Kodi Nelson ayenera kucita ciani?**
   Yankho: ayenera kukhala wodekha ndiponso ayenera kuphunzitsa mkazi wake.

**Bernard ndi Zelipa**

1. **Kodi mudziwa anthu amene amauza anthu ena za mabvuto a m'ukwati?**
   Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.
2. **Kodi Bernard akumva bwanji za mkazi wake, kulingana ndi inu?**
   Yankho: Samvera kulemekezeka, akumva cisoni ndi kutsutsidwa.
3. **Kodi Bernard ayenera kucita ciani?**
   Yankho: Kukhala pansi ndi mkazi wake ndi kumfotokozera cifukwa ciani samvera bwino ngati mkazi wake akamba zambiri. Kumfunsa m'mene alakwa kuti iye angasinthe. Kupemphera pamodzi kuti Mulungu awakhululukire ndi kuwapatsa thandizo kukhala olimba m'ukwati. Sangatume mkazi wake kupita ku makolo ake (onani phunziro 1 za kusiya makolo).

**Cisomo ndi Rakele**

1. **Kodi mudziwa anthu amene anagonana iwo asanakwatirane?**
   Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.
2. **Kodi Baibulo linena ciani za kugonana kunja kwa ukwati?**
   Yankho: Mulungu alola mwamuna ndi mkazi kugonana m'ukwati cabe (Ahebri 13.4). Zinthu zina zonse zichedwa cigololo ndipo siziloleka ndi Mulungu (1 Akorinto 6.18). Mulungu atiuza kukhala ocenjera ngakhale m'njira m'mene tiyang'anira munthu wina (Mateyu 5.28). Mulungu afuna mtima wathu ndi maganizo athu kukhala opanda banga.
3. **Kodi mungapangire Cisomo ndi Rakele kucita ciani?**
   Yankho: Kumbutsani aphunzi za phunziro 1: kusiya – kudziphatikana – kugonana. Cisomo ndi Rakele anagonana (cinthu cacitatu), ndiye anacita cimene Mulungu afuna kucitika m'ukwati cabe. Ayenera kumvera cisoni, kuulula chimo lao ndi kulileka, kupempha Mulungu cikhululukiro ndiponso kuyamba kukhala momwe Mulungu afuna. Cisomo angapangiridwe kumanga ukwati m'njira yoyenera.

**Lemekani and Sara**

1. **Fotokozani cofunikira ca kukhala ndi mwana.**
   Yankho: Ici ndi colinga cina ca ukwati, koma si colinga ceniceni ca miyoyo yathu (phunziro 1). Colinga cathu ndi kumvera ndi kulemekeza Mulunga, anthu akapezeka m'ukwati kapena iai. M'ukwati colinga ndico kukhala monga Mulungu afuna, ngati tili ndi mwana kapena tilibe.
2. **Kodi zifukwa zake za kukhala kopanda mwana ndizo ciani?**
   Yankho: Aloleni kukambirana zifukwa zimene anthu a ku m'mudzi amapereka. Malizitsani pa kunena kuti mwana ndi mphatso yocokera kwa Mulungu. Sitidziwa cifukwa ciani Iye apatsa anthu ena ndipo sapatsa ena. Kungakhale matenda amene apangitsa anthu kusakhala ndi mwana.
3. **Kodi mungapangire Lemekani ndi Sara kucita ciani?**
   Yankho: Kuphunzira kuti mwana ndi mphatso yocokera kwa Mulungu (Salimo 127.3). Sayenera kucita cimene cololeka ndi Mulungu (sayenera kupempha thandizo kwa ng'anga). Ayenera kupempha Mulungu kuwapatsa mwana ndi kunena 'Kufuna kwanu kucitidwe'

**Richard ndi Edina**

1. **Fotokozani cifukwa ciani Richard ndi Edina amakambirana zambiri za ndalama.**
   Yankho: Sabvomerezana za kusewenzetsa bwanji ndalama ndiponso za wamphamvu wa kusewenzetsa ndalama ndiye yani.
2. **Kodi Baibulo litiuza ciani za kusewenzetsa ndalama?**
   Yankho: tiyenera kusewenzetsa ndalama m'njira imene Mulungu afuna, pakuti ndalama ndi zake (Yakobo 1.17).

3. **Kodi mungapangire Richard ndi Edina kucita ciani?**
   Yankho: Kuwerenga Baibulo kudziwa zimene Mulungu akamba za ndalama ndi za kusewenzetsa ndalama: khalani okhutiritsidwa ndi zimene muli nazo (Ahebri 13.5) ndipo khalani akupatsa (Aroma 12.13). Richard sayenera kudzikonda ndi kudzikweza pa kufuna kusunga ndalama m'malo mwa kupatsa zimene banja lisowa. Ayenera kumvetsa kuti m'ukwati ndalama ndi zao osati zake.

**Danieli ndi Dorothy**

1. **Kodi mudziwa anthu amene sakhala pamodzi iwo angakhale ndiwo okwatirana?**
   Yankho: Aliyense ayankhe pa yekha.
2. **Kodi mungapangire ciani Danieli ndi Dorothy?**
   Yankho: Kusakhala pamodzi ngati anthu akwatirana kumabweretsa mabvuto ambiri, ndiye ayenera kuwazindikirako. Ana adzakula kopanda tate wao pafupi, kudzakhala mayesero a kuyamba ubwenzi kunja kwa ukwati ndi zina zotere.

**Amos ndi Selina**

1. **Kodi mungapangire ciani Amos?**
   Yankho: Kuphunzira kudziletsa ndi kupempha Akristu okhwima kumpangira.

- Funsani aphunzi zimene ayenera kucita ngati azindikira kuti anacimwa.
  Yankho: Kuleka kucimwa, kuulula macimo awo kwa Mulungu, kudalira pa Yesu kuti apulumutsidwe.
- Funsani aphunzi ngati 'mankhwala a cikondi' angathandize kuthetsa mabvuto a m'ukwati ndiponso ngati mankhwalawa angapangitse munthu kutikonda.
  Yankho: Iai, sangathandize. M'malo mwa ici kudzakhala: cisinsi, mwamuna/mkazi wokaikira, kutaya kwa kukhulupirana ngati cisinsi cabvumbulutsidwa.

## 3. Malangizo a Mulungu kwa azimuna ndi azimai – kuwerenga Baibulo (40 minutes)

- Werengani pamodzi Aefeso 4.2 ndi 3 ndipo yankhani pamodzi mafunso awa:
  1. **Kodi ndime izi zitiphunzitsa ciani za njira ya kukambirana?**
     Yankho: Tiyenera kukhala okoma mtima, odzicepetsa ndiponso sitiyenera kuika za ife mwini patsogolo.
  2. **Kodi cofunikira koposa ndico kulankhula ndi mwamuna/mkazi pa mabvuto ndi zolakwa kapena kusalankhulana?**
     Yankho: Malinga ndi mabvuto otani. Ngati kusalankhula kudzaononga mgwirizano ndi ciyanjano, kulankhulirako ndi kwabwino koposa kuti anthu akhululukirane ndi kuyanjananso. Ngati bvuto ndi laling'ono ndipo silionongа mgwirizano ndi ciyanjano, mungasankhe kusalankhulirako. Ngati kuli bvuto, osaika mlandu pa wina, koma zindikirani kuti mwina mwaonjezerako.
  3. **Kodi ndime izi zitiphunzitsa ciani za ciyambi ca ciyanjano?**
     Yankho: Cicokera kwa Mulungu. Cifukwa cace Mulungu ayenera kukhala maziko a ukwati.
  4. **Kodi kusunga ciyanjano m'ukwati ndiko cinthu capafupi?**
     Yankho: Nthawi zambiri ndi cinthu cobvuta, pakuti ife anthu ndife odzikonda (ocimwa) m'malo mwa kuganizira zimene azimuna/azimai athu aganiza ndi kulaka. Anthu adziganizira cabe. Kukhala m'ukwati kutanthauza kulimbikira: kuphunzira kumvera azimuna/azimai athu. Akumbutseni: ukwati ndi cipangano pa maso pa Mulungu ndipo ukwati ufunika anthu odzipereka.

- Werengani pamodzi Mlaliki 4.12 ndipo yankhani pamodzi funso iri:
  5. **Kodi ndime iyi ya m'Baibulo itanthauza ciani?**
     Yankho: Anthu amene analandira Yesu kukhala Mpulumutsi wao ali ndi ukwati wolimba kuposa anthu opanda Mulungu: Mulungu awaphunzitsa kukhala acikondi, okhulupirika, odzicepetsa ndi zina zotere monga Iye yemwe aliri.

- Werengani pamodzi 1 Akorinto 13.4-7 ndipo yankhani pamodzi funso iri:
  6. **Werenganinso ndime ya 5. Kodi citanthauza ciani kuti cikondi sicitsata za mwini yekha?**
     Yankho: Kufunafuna zimene munthu wina (mwacitsanzo mwamuna/mkazi) afuna. Kutanthauza kudzikana. Kutanthauza kutsutsa cilakolako conyasa. Kutanthauza kutumikira wina osati iye mwini.

- Werengani pamodzi Yohane 13.34 ndipo yankhani funso iri:
  7. **Cifukwa ciani Yesu ndi citsanzo cathu ca cikondi?**
     Yankho: Iye, monga Mfumu wa mlengamlenga, anadzipereka kuti afe pa mtanda kukhululukira macimo a anthu ake. Anadzikana ndithu! Pamene tidziwa kuti tapulumutsidwa mwa Iye, tidzamvetsa ndi kufuna zimene Yesu acita: kukonda ndithu moonadi ndi mokhulupirika.

- Werengani pamodzi Ahebri 13.4 ndipo yankhani funso iri:
  8. **Kodi Baibulo likamba ciani za kugonana m'ukwati?**
     Yankho: Ndi cabwino kugonana m'ukwati.

- Werengani pamodzi 1 Akorinto 7.3-5 ndipo yankhani mafunso awa:
  9. **Kodi ndime izi zitiphunzitsa ciani za kugonana m'ukwati?**
     Yankho: Kugonana ndiko mphatso ya mgwirizano (cikondi, kudzipereka). Anthu okwatirana saloledwa kukanizana koma cabe akabvomerezana. Ndime iyi ya m'Baibulo siingagwiritsidwe nchito kukakamiza munthu kugona nafe, pakuti pa kucita tero mudzitumikira m'malo mwa kutumikira azimuna/azimai athu (komwe kutsutsa ndi citanthauzo ca ukwati).
  10. **Kodi ndime izi zitiphunzitsa ciani za cigwirizano m'ukwati?**
     Yankho: Ndi cofunikira kwambiri pakuti kukhala amodzi kutanthauza kubvomerezana ndi kubweretsedwa m'mgwirizano. Ngati kulibe cigwirizano ndipo anthu okwatirana afuna kukanizana, iwo ayenera kuthetsa coyambitsa ca kusagwirizana kwao.

- Werengani pamodzi 2 Akorinto 6.14 ndipo yankhani mafunso awa:
  11. **Cifukwa ciani Mulungu atiletsa kukwatira kapena kukwatiwa ndi munthu amene si Mkristu?**
     Yankho: Mkristu sangakhale amodzi ndi amene sali Mkristu cifukwa maganizo ao a za umoyo atsutsana, sagwirizana pa cofunikira ca kupembedza Mulungu, sagwirizana pa njira ya kulera ana ndi zina zotere.
  12. **Kodi ndime iyi itiphunzitsa ciani za cofunikira ca kusankha mwamuna/mkazi wacikristu?**
     Yankho: Ndi cofunikira kwambiri. Osayang'ana maonekedwe a munthu, koma m'mene akhalira moyo wake kwa Mulungu.

## 5. Kutsiriza (5 minutes)

- Bwerezani zimene zaphunzitsidwa lero: ukwati wacikristu utanthauza kutumikirana mogwirizana ndi mwa ciyanjano. Pa kucita tero anthu okwatirana amvera ndi kutumikira Mulungu.
- Pempherani.

## Lesson 3 Azimuna acikristu

Zofunikira pa nthawi ya kuphunzira
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

## 1. Kulandiridwa (10 minutes)
- Landirani onse.
- Pempherani.
- Fotokozani kuti azimuna ndi azimai sasiyana pa maso pa Mulungu: iwo awiri ndiwo ofunikira pa maso pake. Komabe udindo womwe Mulungu awapatsa ndi wosiyana.

## 2. Udindo wa mwamuna – Kuwerenga Baibulo (30 minutes)
- Funsani aphunzi za mwamuna wacikristu: iye ndiye munthu wotani kodi?
  Yankho: Aloleni kupereka mayankho ao. Malizitsani kukambirana pa kunena kuti cofunikira koposa ndi m'mene Mulungu akamba za azimuna ndi maudindo yao.

- Werengani pamodzi 1 Akorinto 11.3 ndipo funsani mafunso awa:
  1. **Citanthauzanji kuti mutu wa nyumba ndiwo mwamuna?**
     Yankho: Mwamuna monga mutu wa nyumba ali ndi udindo wa kutsogolera banja m'njira yabwino. Ici citanthauza kutumikira. Osati kulamulira mwa nkhanza cifukwa olamulira a nkhanza adzitumikira m'malo mwa kutumikira mabanja ao.
  2. **Citanthauzanji kuti Yesu ndi Mutu wa mwamuna?**
     Yankho: Mulungu ali ndi ulamuliro pa mwamuna. Mwamuna saloledwa kucita ciriconse cimene afuna, koma ayenera kucita cifuniro ca Mulungu ca pa mkazi wake (ndi ana ake). Mwa kucita tero, mkazi sangacitidwe konse monga iye ndiye kapolo.

- Werengani Deuteronomo 24.5 ndipo funsani funso iri:
  3. **Kodi udindo woyamba wa mwamuna ndiwo ciani kulingana ndi ndime iyi?**
     Yankho: Kukondweretsa mkazi wake.

- Werengani 1 Petro 3.7 ndipo funsani funso iri:
  4. **Kodi amuna ayenera kukhala ndi akazi ao m'njira yotani?**
     Yankho: Ayenera kuwalemekeza ndi kusacitisa manyazi. Ndiye mwamuna wabwino sadzanyoza mkazi wake.

- Werengani pamodzi Aefeso 5.22-33 ndipo yankhani mafunso awa:
  5. **Kodi Mulungu apatsa lamulo lotani m'ndime ya 25?**
     Yankho: Azimuna ayenera kukonda azikazi ao: kukhala amodzi, ciyanjano ndi cikondano.
  6. **Werenganinso ndime ya 25. Yesu anadzipereka cifukwa ca anthu ake. Kodi citsanzo ici citanthauza ciani kuli amuna?**
     Yankho: Kusakhala odzikonda koma kutumikira azikazi ao.
  7. **Werenganinso ndime ya 29. Kodi amuna ayenera kucita ciani kulingana ndi ndime iyi?**
     Yankho: Kupatsa azikazi ao zonse zimene asowa ndiponso kuimira m'malo mwa Mulungu m'banja (m'njira yotero kuti banja aphunzira za Mulungu poona mwamuna/tate). Cifukwa ca ici azimuna afunika Yesu: kopanda Iye iwo sakhoza kuimira m'malo mwa Mulungu. Kusamalira azikazi ao monga Yesu asamalira anthu ake (amene ali agonthi, osowa njira ndi kutayika m'uzimu nthawi zambiri).
- Malizitsani pa kunena kuti maudindo a mwamuna ndiwo:
  1. Kukonda mkazi wake 2. Kusamalira banja 3. Kuteteza banja

## 3. Udindo wa mwamuna – moyo wa masiku onse (30 minutes)

- Lembani pa bolodi: **Za thupi**. Funsani aphunzi maganizo ao pa m'mene mwamuna ayenera kusamalira zosowa za thupi za mkazi wake (ndi za ena a m'banja). Kambiranani pamodzi mayankho ao. Zitsanzo: nchito, kugula zobvala/sopo/zofunikira za ku sukulu, kusaononga ndalama.
- Lembani pa bolodi: **Kupanga maganizo**. Funsani aphunzi maganizo ao pa m'mene mwamuna monga mutu wa nyumba ayenera kupanga maganizo. Kambiranani pamodzi mayankho ao. Zitsanzo: ayenera kudziwa zosowa za mkazi wake, kumfunsa maganizo ake, kutsimikizira kuti zikonzero zitumikira mkazi ndi ana osati mwamuna poyamba. Ngati sagwirizana: mkazi ayenera kudzipereka kwa mamuna wake ndipo mwamuna wabwino adzayesa kukondweretsa mkazi wake nthawi zonse.
- Lembani pa bolodi: **Umoyo wauzimu**. Funsani aphunzi maganizo ao pa m'mene mwamuna ayenera kutsogolera mkazi wake ndi ana ao m'moyo wauzimu (osaya kwambiri pakuti izi zonse zidzakambidwiranso m'phunziro 6). Kambiranani pamodzi mayankho ao. Zitsanzo: kukhala wofunikira kwambiri pa nkhani ya Baibulo, kutenga banja ku calichi, kukhala citsanzo cabwino.
- Lembani pa bolodi: **Miyambo**. Funsani aphunzi maganizo ao pa m'mene mwamuna ayenera kutsogolera ndi kutumikira mkazi wake ndi ana ao pa nkhani ya miyambo (osaya kwambiri, pakuti izi zonse zidzakambidwiranso m'phunziro 5). Kambiranani pamodzi mayankho ao. Zitsanzo: kudziwa, kutenga ulamuliro pa zimene anyamata ndi atsikana aphunzitsidwa ndiponso pa kuwaphunzitsa ndi yani (mwambo wa ndola, udindo wa agogo), kuyeretsedwa kwa mkazi/mwamuna wa masiye, miyambo atabadwa mwana.

## 4. Zolowapo (30 minutes)

- Gawani gulu m'magulu ang'ono ndipo patsani gulu lirilonse colowapo cimodzi kuti akambireko. Kapena kambiranani pamodzi zolowapo zonse.

**Zolowapo**

**1. Dalitso**

Dalitso anakwatira Felicia caka catha. Sakhala wokhazikika pa mbali ya kukhala mwamuna wabwino, pakuti tate wake sanali citsanzo cabwino m'banja lake. Anzake a Dalitso amuuza kuti iye ndiye bwana wa banja, cimene citanthauza kuti mkazi wake ayenera kumtumikira ndi kumkondweretsa m'ciriconse cimene afuna. Pamene Dalitso ananena kuti afuna kucita ciriconse kukondweretsa mkazi wake, anzake amamseka. Dalitso safuna kuganizirabe. Apanga maganizo za kumwa mowa ndi kusangalala cabe.

1. Kodi Dalitso ndi mwamuna wabwino? Cifukwa ciani mwayankha tero?
2. Kodi Dalitso ayenera kucita ciani?
3. Kodi Felicia angacite ciani kuthandiza mwamuna wake kucita bwino koposa?

**2. Albert**

Albert ali ndi zaka 27. Anakwatira Grace ndipo iwo ali ndi ana atatu. Masiku onse Albert amapita ku Petauke kucita business. Grace sadziwa kuti amacita business yotani. Adziwa cabe kuti Albert alephera kupatsa zimene banja lisowa. Patapita nthawi, mnzake wa Grace amuuza kuti Albert amangoyendayenda ndi kusewera nsolo ku boma. Pamene Grace amfunsa Albert, iye ayankha, 'Ndi cofunikira kwambiri kukomana ndi anthu ndiponso kupeza abwenzi. Anzanga akamba kuti adzandithandiza. Timasewera masewero kuti tidziwane. Tsogolo lathu lidzakhala labwino kwambiri'.

1. Kodi Albert ndi mwamuna wabwino? Cifukwa ciani mwayankha tero?
2. Kodi Albert ayenera kucita ciani?
3. Kodi Grace angacite ciani kuthandiza mwamuna wake kucita bwino koposa?

**3. Masauso**

Masauso anakwatira Mercy. Iwo ali ndi ana amuna asanu ndi awiri. Masauso ndi Mercy amayambana kwambiri za njira ya kulera ana ao. Masauso akamba nthawi zonse, 'Ine ndine

mwamuna. Ndidziwa zimene anyamata afunika. Simudziwa pakuti ndinu mkazi. Ndifuna anyamata anga kukhala monga ine, ndiye ayenera kucita ciriconse cimene ndinena ndipo inu muyenera kukhala cete'. Nthawi ina Masauso apatsa lamya kwa Paulo, mwana wao woyamba wa mwamuna. Paulo aleka kuikako nzeru ku sukulu. Mercy afuna Paulo kumpatsa lamya kuti alisunge, koma mwamuna wake Masauso akamba kuti si nchito yake.

1. Kodi Masauso ndi mwamuna wabwino? Cifukwa ciani mwayankha tero?
2. Kodi Masauso ayenera kucita ciani?
3. Kodi Mercy angacite ciani kuthandiza mwamuna wake kucita bwino koposa?

**4. Emmanuel**

Emmanuel anakwatira Zenia. Iwo ali ndi ana awiri. Emmanuel analephera kupeza nchito. Zenia ndi wophika ku malo odyeramo. Zenia saona, agawa ndalama pamodzi ndi mwamuna wake ndipo sakhala odzikudza. Emmanuel akumva monga alephera kukhala mwamuna wabwino ndipo akumva nsanje kuli mkazi wake. Tsiku lina akomana ndi mkazi amene amsamalira mwapadera. Emmanuel akondwera kwambiri za momwe iye amsamalira. Iye ayamba kuyenda naye m'tseri.

1. Kodi Emmanuel ndi mwamuna wabwino? Cifukwa ciani mwayankha tero?
2. Kodi Emmanuel ayenera kucita ciani?
3. Kodi Zenia angacite ciani kuthandiza mwamuna wake kucita bwino koposa?

**5. Eneas**

Eneas ali m'ukwati ndi Gertrud zaka makumi atatu. Iwo ali ndi ana anai. Eneas akamba kuti, 'Ndikonda mkazi wanga. Cimene ndifuna ndi kumkondweretsa. Ndimacita ciriconse cimene ndikhoza kusamalira mkazi wanga ndi ana athu. Pamene ndiona kuti mkazi wanga sakondwa, ndiyesa kufufuza ngati ndalakwa ndipo ndipempha mkazi wanga cikhululukiro. Nthawi zonse pamene sitigwirizana, tikambirana. Sindimenya mkazi wanga. Ndidziwa kuti Mulungu andikhululukira macimo anga onse ndipo ndifuna kucitira cifundo mkazi wanga monga Mulungu andicitira cifundo. Nthawi zina ndiletsa ana anga cinthu cimene cingawakopere m'njira yoipa, mwacitsanzo nyimbo zoipa. Ife monga banja tifuna kumvera Mulungu yekha. Timapembedza Mulungu usiku uliwonse, pakuti ndifuna ena kudziwanso Yesu monga Mpulumutsi wao. Ndikumva kuti ndiri ndi udindo kuwapangitsa kukhala odziwa bwino Baibulo.

1. Kodi Eneas ndi mwamuna wabwino? Cifukwa ciani mwayankha tero?
2. Kodi Gertrud angacite ciani kuthandiza mwamuna wake kucita bwino koposa?

- Mayankho abwino ali conco:

  **Dalitso**

  1. **Kodi Dalitso ndi mwamuna wabwino? Cifukwa ciani mwayankha tero?**
     Yankho: Dalitso afuna kukhala mwamuna wabwino koma sali wabwino. Aopa kutenga ulamuliro: aganiza kuti sadziwa kukhala bwanji mwamuna wabwino. Ndipo aopa mau a anzake. Pofuna kupeza yankho ayesa kuiwala zonse ndi kumwa mowa, koma kumwa mowa sikuthetsa bvuto.
  2. **Kodi Dalitso ayenera kucita ciani?**
     Yankho: Kukhala woima nji, kuwerenga Baibulo ndi kulankhula ndi Akristu pa mfundo izi. Koma kuposa zonse ayenera kukonda Mulungu: kudziwa Mulungu kudzakulitsa cilakolako ca kukondweretsa Mulungu ndi kucita zimene Iye afuna Dalitso kucita kuti atumikire mkazi wake.
  3. **Kodi Felicia angacite ciani kuthandiza mwamuna wake kucita bwino koposa?**
     Yankho: Kuonetsa kuti amkhulupirira mwa kumlimbikitsa kukhala monga Mulungu afuna: mutu wotenga ulamulira pa nyumba.

  **Albert**

  1. **Kodi Albert ndi mwamuna wabwino? Cifukwa ciani mwayankha tero?**
     Yankho: Si ndiye mwamuna wabwino. Sapatsa banja zosowa zake. Sasamalira banja. Komatu saganizirako. Ici citanthauza kuti Albert ndi waulesi.

2. **Kodi Albert ayenera kucita ciani?**
   Yankho: Kukhala wolimba, kupeza njira ya kupeza ndalama (kulima, kucita nchito ya ganyu kapena malonda) m'malo mwa kusewera cabe. Kupempha Mulungu thandizo kucita zabwino.
3. **Kodi Grace angacite ciani kuthandiza mwamuna wake kucita bwino koposa?**
   Yankho: Kulimbikitsa Albert kutenga ulamuliro. Kumthandiza kupeza nchito kapena nchito ya ganyu.

**Masauso**

1. **Kodi Masauso ndi mwamuna wabwino? Cifukwa ciani mwayankha tero?**
   Yankho: Si wabwino. Safuna kumvera maganizo a mkazi wake ndipo iye ndiye wodzikonda. Anali kudzikweza kwambiri kuti angamvere. Sanateteze banja lake ku magwero oipa (foni)
2. **Kodi Masauso ayenera kucita ciani?**
   Yankho: Ayenera kumvetsa kuti udindo wake ndiwo kutumikira banja osati iye mwini ndiponso kuti iye ali ndi udindo wa kuteteza banja.
3. **Kodi Mercy angacite ciani kuthandiza mwamuna wake kucita bwino koposa?**
   Yankho: Kuonetsa mwamuna wake kuti amkonda ndi kumlemekeza. Kuonetsa cikhululukiro pa colakwa. Kusanyoza ndi kusacita mjedo.

**Emmanuel**

1. **Kodi Emmanuel ndi mwamuna wabwino? Cifukwa ciani mwayankha tero?**
   Yankho: Anayesa kukhala mwamuna wabwino. Sanalakwe pa kusapeza nchito koma analakwa pa kuyamba kuyenda ndi mkazi wina m'tseri.
2. **Kodi Emmanuel ayenera kucita ciani?**
   Yankho: Kulapa chimo lake, kuuza mkazi wake za kamvekedwe kwake kwa kulephera ndiponso kuyanjananso ndi mkazi wake (ngati mkazi afuna kumsiya, aloledwa kucita tero cifukwa ca cigololo ca mwamuna wake). Emmanuel ayenera kumvetsa kuti Mulungu anampatsa mkazi wake kumthandiza.
3. **Kodi Zenia angacite ciani kuthandiza mwamuna wake kucita bwino koposa?**
   Yankho: Kumfotokozera kuti kulephera kupeza nchito sikutanthauza kuti iye analakwa, pakuti anayesadi. Mwa kucita tero, Zenia amlemekeza ndipo Emmanuel adzamva bwino. Ayenera kupemphera pamodzi kuti Mulungu awathandize. Zenia ayenera kuthandiza Emmanuel kupeza nchito ya ganyu kapena malonda.

**Eneas**

1. **Kodi Eneas ndi mwamuna wabwino? Cifukwa ciani mwayankha tero?**
   Yankho: Inde, Eneas ndi mwamuna wabwino. Akonda mkazi wake, ateteza banja, awasamalira ndipo iye ndiye citsanzo ca kutumikira Mulungu.
2. **Kodi Gertrud angacite ciani kuthandiza mwamuna wake kucita bwino koposa?**
   Yankho: Kumthandiza ndi kumlimbikitsa kutumikira banja mwa kudzipereka kwa mwamuna wake.

## 5. Kutsiriza (5 minutes)

- Bwerezani mwacidule phunziro la lero.
- Kambaninso kuti udindo wa mwamuna ndiwo kutumikira Mulungu mwa kukonda mkazi wake ndi kuteteza ndi kusamalira banja.
- Pempherani.

## Phunziro 4 Azimai acikristu

Zofunikira pa nthawi yophunzira
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

# 1. Kulandiridwa (10 minutes)
- Landirani onse.
- Pempherani.
- Bwerezani mwacidula zimene zinaphunzitsidwa m'maphunziro apitao: ukwati ndi mphatso ya Mulungu ndipo udindo wa azimuna ndiwo kulemekeza Mulungu mwa kutumikira azikazi ao ndi ana ao.

# 2. Udindo wa mkazi – Kuwerenga Baibulo (30 minutes)
- Funsani aphunzi kuti udindo wa azimai a m'ukwati ndiwo ciani. Kodi mkazi ayenera kukhala munthu wotani ndipo ayenera kucita ciani?
- Werengani pamodzi Aefeso 5.22 ndipo funsani aphunzi funso iri:
  1. **Kodi Mulungu alamulira ciani akazi?**
     Yankho: Kudzipereka kwa azimuna ao: kumvera ndi kupereka ulemu mwa mtima wodekha ndi wofatsa. M'zinthu zonse pokhapokha ngati azimuna ao afuna iwo kucimwa. Kudzipereka kwa azimuna ao monga adzipereka kwa Mulungu, pakuti azimuna ao apatsidwa kukhala mitu yao.

- Werengani pamodzi Tito 2.3-5 ndipo yankhani pamodzi mafunso awa:
  2. **Kodi udindo wa akazi okalamba ndiwo ciani?**
     Yankho: Kuphunzitsa zabwino ndi kukhala zitsanzo zabwino za azikazi ang'ono (ndime za 4 ndi 5).
  3. **Kodi udindo wa akazi ang'ono ndiwo ciani?**
     Yankho: Zonse zolembedwa m'ndime za 4 ndi 5. Kambiranani pamodzi citanthauzo ca ubwino uwu uliwonse m'umoyo wa masiku onse. Auzeni kuti sitikwaniritsa kucita ubwino m'mphamvu yathu koma tifunika Mulungu.

- Werengani pamodzi Miyambi 31.10-31. Uzani aphunzi kukhala m'magulu ang'ono kukambirana mafunso awa omwe mulemba pa bolodi. Kapena kambiranani pamodzi.

| **Mafunso** |
|---|
| 4. Werenganinso ndime ya 12. Kodi akazi ayenera kucita ciani? |
| 5. Kodi ndime izi za m'Baibulo zitiphunzitsa ciani kuli akazi aulesi? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho? |
| 6. Kodi akazi abwino amatumikira amuna ao ndi mabanja ao m'njira zotani? Ndi m'ndime ziti mwapeza yankho? |
| 7. Werenganinso ndime ya 20. Kodi akazi abwino amacita ciani kupanda kutumikira amuna ao ndi mabanja ao? |
| 8. Werenganinso ndime ya 23. Kodi cingaoneke bwanji ngati mwamuna ali ndi mkazi wabwino? |
| 9. Kodi mkazi angathandize mwamuna wake kupeza ndalama? |
| 10. Kodi Baibulo litiphunzitsa ciani m'Miyambi 31.30 za cofunikira ca maonekedwe? |

- Mayankho abwino ali conco:
  4. **Werenganinso ndime ya 12. Kodi akazi ayenera kucita ciani?**
     Yankho: Ayenera kucita zabwino nthawi zonse.

5. **Kodi ndime izi za m'Baibulo zitiphunzitsa ciani kuli akazi aulesi? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?**
   Yankho: Iwo saliri monga cifuniro ca Mulungu. Azimai ayenera kukhala ocenjera kutumikira azimuna ao ndi mabanja ao.
6. **Kodi akazi abwino amatumikira amuna ao ndi mabanja ao m'njira zotani? Ndi m'ndime ziti mwapeza yankho?**
   Yankho: Mwa kugwira nchito molimba, kukonzekera cakudya, kucita nchito yao kopanda cibwana, kuthandiza kupeza ndalama, kukhala okoma mtima, kusamalira nyumba.
7. **Werenganinso ndime ya 20. Kodi akazi abwino amacita ciani kupanda kutumikira amuna ao ndi mabanja ao?**
   Yankho: Athandiza wina aliyense wobvutika.
8. **Werenganinso ndime ya 23. Kodi cingaoneke bwanji ngati mwamuna ali ndi mkazi wabwino?**
   Yankho: Mkazi wabwino athandiza mwamuna wake m'kupambana kwake (m'Cipangano Cakale anthu ankakomana kubwalo kumene ankacita malonda komanso kumeneko kunali bwalo la milandu, ndiye anthu ofunikira ndi anthu opambana anapezeka pabwalo).
9. **Kodi mkazi angathandize mwamuna wake kupeza ndalama?**
   Yankho: Inde, angathandize (ndime ya 24).
10. **Kodi Baibulo litiphunzitsa ciani m'Miyambi 31.30 za cofunikira ca maonekedwe?**
    Yankho: Makhalidwe ndi mtima ndizo zofunikira zoposa maonekedwe: mkazi amene aopa Mulungu. Mkazi wotere adzacita zatheka kuti atumikire Mulungu mwa kumvera mwamuna wake ndi kutumikira banja lake.

## 3. Udindo wa azikazi – umoyo wa masiku onse (15 minutes)

- Mkazi aima pafupi ndi mwamuna wake. Sasiyana pa kufunika kwao. Mkazi athandiza, alimbikitsa ndi kutonthoza (kusekeretsa) mwamuna wake pa kuitanidwe kwake kwa Mulungu: kutumikira Mulungu ndi banja.
- Udindo woyamba wa mkazi ndiwo kutumikira Mulungu, waciwiri mwamuna wake, wacitatu ana ake ndipo potsiriza anthu ena (makolo/abale/anthu opezeka pafupi). Udindo wake woyamba ndiwo pa nyumba. Udindowu ndi wofunikira kwambiri: mwa kucita tero, atumikira Mulungu!
- Mkazi angacite mantha kuti mwamuna wake alakwa, cimene ciri cotheka ndithu. Ici cimubvutitsa kumvera mwamuna wake. Ayenera kumvetsa kuti nchito yake ndi kumvera. Ayenera kuphunzira kukhala wokhulupirika ndi kukhulupirira mwamuna wake. Kumbukirani: kupezeka m'ukwati kutanthauza kulimbika ndi kucita zonse zatheka.

## 4. Zolowapo (30 minutes)

- Uzani aphunzi kukhala m'magulu ang'ono ndipo patsani gulu lirilonse colowapo cimodzi kuti akambiraneko. Kapena awerengereni zolowapo ndipo kambiranani pamodzi.

**Zolowapo**

**1. Josines**

Josines ndi wokwatiwa ndi Edson. Edson amayesa kutumikira bwino banja lake monga akhoza. Pamene azindikira kuti alakwa, apempha cikhululukiro ndipo ayesa kucita bwino koposa. Koma Josines akonda kuuza anzake zolakwa zonse za Edson pamene iwo apita kutapa madzi. Josines alephera kukhululukira ndi kukhulupirira kuti Edso adzacita bwino koposa m'tsogolo.

1. Kodi Josines ndi mkazi wabwino? Cifukwa ciani mwayankha tero?
2. Kodi Josines angacite ciani kuti acite bwino koposa?
3. Kodi Edson angacite ciani kuthandiza mkazi wake kucita bwino koposa?

**2. Anastazia**

Anastazia ali ndi zaka makumi atatu. Akwatiwa ndi Milan ndipo iwo ali ndi ana ang'ono awiri. Anastazia akonda kusamalira anthu obvutika. Ku calichi ali m'mbali ya anthu amene amasamalira

anthu okalamba. Atsogoleri a mpingo amuyamikira kwambiri cifukwa ca nchito imene Anastazia amacita. Komabe, nthawi zambiri afika mocedwa kunyumba ndipo alephera kucapa bwino zobvala. Milan sakondwera poona kuti nchito zilipo pamene afika kunyumba atagwira ganyu. Apita kwa atsogoleri a mpingo kuwapempha upangiri.

1. Kodi Anastazia ndi mkazi wabwino?
2. Kodi Anastazia angacite ciani kuti adzacita bwino koposa?
3. Kodi Milan angacite ciani kuthandiza mkazi wake kucita bwino koposa?

**3. Veronica**

Veronica ndi wokwatiwa ndi Acklas. Iwo ali ndi ana asanu. Cioneka kuti Acklas amapeza colakwa kuti angacite ndeu. Veronica anayesa kufufuza cifukwa ca ndeu, koma Acklas sapatsa yankho lirilonse. Nthawi zina Acklas amumenya. Veronica akumva kuti ali yekha ndipo aopa kuti tsiku lina Acklas angapweteke ana. Veronica sadziwa kucita ciani. Aganiza kuti mwina kungakhale bwino kupeza mwamuna wina.

1. Kodi Veronica ndi mkazi wabwino?
2. Kodi mungapangire ciani Acklas?
3. Kodi mungapangire Veronica kucita ciani?

**4. Catherine**

Catherine ndi wokwatiwa ndi Sekelani. Iwo alibe ana, angakhale ali m'ukwati zaka zambiri. Catherine amakonda Sekelani, koma sakonda nchito ku nyumba. Akamba kuti sakonda kutsuka mbale ndi kucapa zobvala. Afuna nchito yoona, monga mnzake amene amagwira nchito pa malo omwetsera mafuta. Catherine akamba, 'Nchito ku nyumba si zofunikira kwambiri. Ndifuna kukhala munthu wofunikira kwambiri. Ndimangocapa, ndimangotsuka ndi kuphika masiku onse, kwatha.'

1. Kodi Catherine ndi mkazi wabwino?
2. Kodi Catherine angacite ciani kuti adzacita bwino koposa?
3. Kodi Sekelani angacite ciani kuthandiza Catherine kucita bwino koposa?

**5. Mulumbenji**

Mulumbenji ndi mkazi wokalamba wa zaka makumi asanu ndi awiri. Anena, 'Pamene ndinali wamg'ono, ndinali wokwatiwa ndi Tyson. Tinali okondwa pamodzi. Ndinafuna kuti Tyson anali munthu wokondwera woposa m'dziko lonse lapansi. Ndipo iye anafuna kuti munthu wokondwera woposa ndine. Tyson anandicitira bwino. Ndinali wacisoni kwambiri pamene iye anamwalira. Ndinakonda kumsamalira: kuphika, kucapa zobvala zake ndi kusamalira nyumba kuti ioneka bwino ndi yotsetseka. Iye analibe nchito, koma anacita zonse zimene akhoza kutipatsa zimene tinasowa. Tyson anali wokoma mtima kuli ana athu. Tinawalera pamodzi. Tsopano ndikonda kuphunzitsa akazi ang'ono njira ya kukhala ndi amuna ao kulingana ndi Baibulo. Ndifuna kuthandiza pa zimene angacite m'miyambo ya cikhalidwe imene itsutsana ndi Baibulo. Ico ndi cimene ndinaphunzira kwa mwamuna wanga. Sindingamuiwale nthawi zonse.'

1. Kodi Mulumbenji ndi mkazi wabwino, mai wabwino ndi gogo wabwino?
2. Kodi anthu a m'banja ndi a m'mudzi ayenera kuyankha bwanji maphunzitsidwe a Mulumbenji?

- Itatha 10 minutes, kambiranani pamodzi mayankho. Mayankho abwino ali conco:

  **Josines**

  1. **Kodi Josines ndi mkazi wabwino? Cifukwa ciani mwayankha tero?**
     Yankho: Acita bwino ku mbali ya kusamalira nyumba, koma sakhala bwino ndi mwamuna wake.
  2. **Kodi Josines angacite ciani kuti acite bwino koposa?**
     Yankho: Kukhulupirira mwamuna wake, kumlimbikitsa ndi kumtandiza kucita bwino koposa ndi kumpatsa ulemu. Kuleka kulankhula ndi anzake za zolakwa za mwamuna wake. Kukhala ofuna kukhulukira.

3. **Kodi Edson angacite ciani kuthandiza mkazi wake kucita bwino koposa?**
   Yankho: Kupitiriza kumuonetsa cikondi cake ndi cisamaliro cake. Kupemphera pamodzi. Kuwerenga Baibulo pamodzi pa zimene Mulungu afuna azimai kucita (osagwiritsa nchito Baibulo kulanga kapena kunyoza mkazi wanu, koma waphunzitseni modzicepetsa kucita bwino koposa).

**Anastazia**

1. **Kodi Anastazia ndi mkazi wabwino?**
   Yankho: Acita bwino ku mbali ya kusamalira anthu obvutika, koma sacita bwino ku mbali ya kusamalira mwamuna wake ndi ana ake.
2. **Kodi Anastazia angacite ciani kuti adzacita bwino koposa?**
   Yankho: Kuphunzira kuti udindo wake woyamba uli pa nyumba: mwamuna wake ndi ana ake.
3. **Kodi Milan angacite ciani kuthandiza mkazi wake kucita bwino koposa?**
   Yankho: Kuwerenga Baibulo pamodzi pa zimene Mulungu afuna azimai kucita (osagwiritsa nchito Baibulo kulanga kapena kucititsa manyazi mkazi wanu koma waphunzitseni modzicepetsa kucita bwino koposa). Pempherani pamodzi. Pitani kwa atsogoleri a mpingo kuwafotokozera bvuto ndi kupeza yankho pamodzi.

**Veronica**

1. **Kodi Veronica ndi mkazi wabwino?**
   Yankho: Veronica ndi mkazi wabwino pakuti afuna kusangalatsa mwamuna wake ndi kusamalira ana ake. Komanso si mkazi wabwino pakuti afuna kuthetsa ukwati.
2. **Kodi mungapangire ciani Acklas?**
   Yankho: Kuleka kumenya mkazi wake. Kudziwa mkazi wake kotero kuti adziwa zimene mkazi wake akumva ndiponso zimene afuna. Kuphunzira kutumikira mkazi wake.
3. **Kodi mungapangire Veronica kucita ciani?**
   Yankho: Kufufuza cimene cikwiyitsa mwamuna wake, kukhala okhulupirika, kupemphera, kulankhula ndi anthu amene angampangire ndi kumthandiza. Ngati mwamuna wake apitiriza ndipo kukhala pamodzi ndi koopsya, Veronica angapemphe thandizo kwa apolisi.

**Catherine**

1. **Kodi Catherine ndi mkazi wabwino?**
   Yankho: Mbali yabwino ndi kuti akonda mwamuna wake. Mbali yoipa ndi kuti sakonda udindo wake wa kukhala mkazi.
2. **Kodi Catherine angacite ciani kuti adzacita bwino koposa?**
   Yankho: Ayenera kuphunzira kuti kucita nchito ya kunyumba ndiko njira ya kukondweretsa Mulungu pakuti nchitoyi itumikira mwamuna. Nchitoyi ndi yofunikira monga nchito ina iriyonse imene tingacite kukondweretsa Mulungu nayo. Tiyenera kulemekeza ndi kuyamikira Mulungu m'zonse zimene ticita (Akolose 3.17, 1 Akorinto 10.31).
3. **Kodi Sekelani angacite ciani kuthandiza Catherine kucita bwino koposa?**
   Yankho: Kumuuza ndi kumuonetsa kuti Catherine ndi wofunikira kwambiri ndi nchito imene acita kunyumba ndi yofunikira kwa iye komanso kumpezera njira kuti angakondwere, mwacitsanzo mwa kuthandiza anthu ena a ku mudzi, udindo wa ku calichi kapena nchito imene Catherine angacite kupanda kutumikira mwamuna wake kunyumba.

**Mulumbenji**

1. **Kodi Mulumbenji ndi mkazi wabwino, mai wabwino ndi gogo wabwino?**
   Yankho: Inde. Amvetsa kufunikira kwa kukhala mkazi wacikristu, mai wacikristu ndi gogo wacikristu. Adziwa njira ya kutumikira ndi kuphunzitsa Baibulo ku m'badwo ikudza.
2. **Kodi anthu a m'banja ndi a m'mudzi ayenera kuyankha bwanji maphunzitsidwe a Mulumbenji?**
   Yankho: Ayenera kumlemekeza ndi kumumvera, makamaka cifukwa maphunzitsidwe ake akhala cabe pa Baibulo, citsogozo cathu cokha.

## 5. Kutsiriza (5 minutes)

- Bwerezani mwacidule phunziro la lero.
- Kambaninso kuti udindo wa mkazi ndi kuthandiza mwamuna wake pa kuitanidwa kwake kutumikira banja.
- Pempherani.

## Phunziro 5 Makolo acikristu monga zitsanzo

<u>Zofunikira pa nthawi ya kuphunzira</u>
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

## 1. Kulandiridwa (5 minutes)
- Landirani aphunzi.
- Pempherani.
- Bwerezani mwacidule zimene zinaphunzitsidwa m'maphunziro apitao: ukwati utanthauza ciyanjano, mwamuna ayenera kutumikira banja lake mwa kuimirira m'malo mwa Mulungu m'banja ndipo mkazi ayenera kuthandiza mwamuna wake pa udindo wake wa kutumikira banja.

## 2. Kudziwitsa mutu wa lero (10 minutes)
- Uzani aphunzi kuganiza za makolo ao (kapena ena amene anawalera kapena makolo a m'mudzi) ndipo afunseni kuti iwo anali zitsanzo zotani (zabwino ndi zoipa).
- Ana asanapite ku sukulu aphunzira zambiri. Osati kulankhula, kudya ndi kumvera cabe, komanso za m'mene tikhalira: mamembala a m'banja ndi maudindo ao, kusiyanitsa kwa zabwino ndi zoipa, miyambo, njira ya kukambirana ndi zina zotere.
- Malizitsani ndi kunena kuti makolo ndiwo zitsanzo za m'mabanja ao ndi m'midzi yao, ngakhale ngati safuna kukhala zitsanzo. Ici ndi udindo waukulu!

## 3. Sewero (15 minutes)
- Werengerani aphunzi ziganizo izi. Ngati abvomereza ndi ciganizo, ayenera kukweza dzanja. Ngati sabvomereza, sayenera kukweza dzanja. Aloleni kufotokozera mayankho ao.
  1. **Colinga ca kukhala ndi ana ndico kuti adzatisamalira pamene ife takalamba**
     Yankho: Bodza. Ana angathandize ife ndi mabanja athu, koma kuthandiza si colinga cao: iwo ayenera kuphunzira kumvera, kutumikira ndi kulemekeza Mulungu amene ali Mwini wa miyoyo yao.
  2. **Ana si athu, koma a Mulungu.**
     Yankho: Zoona (Salimo 127.3, Yesaya 8.18). Cifukwa ca ici, makolo ayenera kuwalera m'mene Mulungu afuna. Nthawi zambiri mphatso zisamalika bwino: citani cimodzimodzi ndi ana anu!
  3. **M'Baibulo ana ali ofunikira kwambiri.**
     Yankho: Zoona. Yesu anagwiritsa nchito ana kukhala citsanzo kuti aphunzitse makolo (mwacitsanzo Mateyu 18.5 ndi Macitidwe a Atumwi 2.39). Ana ali ofunikira monga makolo, koma udindo wao usiyana ndi udindo wa makolo.
  4. **Ana afunika cabe cakudya ndi zobvala.**
     Yankho: Bodza. Afunika cikondi, cisamaliro ndi thandizo. Afunika kuphunzitsidwa za kumvera Mulungu ndi makolo ao.
  5. **Ana amaphunzira zambiri za kuyang'ana makhalidwe athu kuposa kumvera mau athu.**
     Yankho: Zoona. Ana atengera ife. Adziwa ngati makhalidwe athu asiyana ndi mau athu.
  6. **Kulibe kusiyana pakati pa makolo acikristu ndi makolo amene si acikristu.**
     Yankho: Bodza. Maziko a kuleredwe kwacikristu ndiko Kristu. Makolo acikristu alera ana ndi cilakolako kusangalatsa Mulungu. Baibulo ndilo lolondolero lao. Ngati kulibe kusiyana, makolo acikristu salera moyenerera ana ao.

## 4. Kusamalira ana opatsidwa ndi Mulungu (15 minutes)
- Funsani aphunzi zimene ana afunika kuti akule bwino. Lembani mayankho ao pa bolodi.

Yankho: Poyamba, ana afunika nyumba yabwino yokhalamo banja lofuna kukhala monga cifuniro ca Mulungu. Ayenera kuphunzitsidwa pa kutumikira Mulungu mwa kukhala moyo wotenga ulamuliro. Zinthu zimene ayenera kuphunzira zidalira pa misinkhu yao, koma afunika thandizo ndi maphunziro:

- Za pa thupi: cakudya, cakumwa, citetezo, zobvala, nyumba, cinjirizo, tulo, mankhwala.
- Za pa zokhudza: kuphunzira za kuthana ndi zokhudza zao (mwacitsanzo mkwiyo, mantha, cimwemwe, cisoni) ndiponso za anthu ena.
- Za mugulu: kuphunzira kumvetsa za dziko lapansi (cikhalidwe), njira ya kusewenzetsa ndalama, njira ya kukhala ndi anthu (kupanga abwenzi, kuthetsa mabvuto ndi zina zotere) ndiponso zina zimene afunika kuti akule kukhala akulu okhala bwino m'mugulu la anthu.
- Za uzimu: kudziwa Mulungu mwa Yesu Kristu, kukhala bwanji miyoyo yao ku ulemerero wa Mulungu ndiponso kukhala okonzeka kuphunzitsa ana ao (phunziro 7).

## 4. Mabanja akunja (15 minutes)

- Funsani aphunzi kuti ndi yani amene ali ndi udindo wa kusamalira mwana m'zosowa zake za thupi, za pa zokhudza, za mugulu ndi za uzimu.
  Yankho: makolo amene anabala mwanayo ali ndi undindo woyamba wa kusamalira mwana, pakuti Mulungu anapatsa iwo mwana wao. Makolo ali ndi mphamvu kuphunzitsa ana ao.
- Kambiranani za udindo wa banja lakunja ndiponso za zocitika m'zimene ana angaleredwe ndi anthu ena amene si makolo a mbadwo.
- Yankho: Nenetsani kuti makolo a mbadwo ali ndi udindo woyamba wa pa ana ao. Banja la kunja liribe mphamvu, koma angathandize kapena kupangira. Ndi cotheka kuti makolo abvutika pa kulera ana ao kotero kuti ana sasamalidwa bwino za pa thupi, za pa zokhudza, za mugulu ndi za uzimu. Ngati ziri tero, mamembala ena a banja angathandize, mwacitsanzo mwa kusamalira mwana. Ngati tilola ana athu kuleredwa pa nyumba ina, tiyenera kudziwa kuti:
  - Tiyenera kukhala maso kuti tipereka kwa yani udindo wa kulera ana athu. Ngati ana athu aleredwa ndi anthu ena, anthuwo ndiwo amene adzawaphunzitsa ndi kuongola makhalidwe ao.
  - Colinga cacikulu ca ana si kuti akhale akapolo athu (komabe angatithandize).
  - Ana ambiri adzalakalaka kukhala ndi makolo amene anawabala. Cilakolakoci cingabvute mwana komanso ubale pakati pa ana ndi owasunga.

## 5. Kuwerenga Baibulo (30 minutes)

- Uzani aphunzi kuyankha mafunso awa m'magulu ang'ono. Lembani mafunso pa bolodi.

**Mafunso**

Aefeso 4.25-32

1. Werenganinso ndime ya 25. Kodi makolo ayenera kucita ciani kulingana ndi ndime iyi?
2. Kodi tiloledwa kukalipa?
3. Kodi mudziwa makolo amene anena zoipa (ndime ya 31)?
4. Werengani ndime ya 32. Citanthauzanji kukhala okoma wina ndi mnzace?

1 Atesalonika 5.15

5. Kodi tiyenera kucita ciani kulingana ndi ndime iyi?
6. Kodi kutsatira cokoma kutanthauza ciani?
7. Kodi ndime iyi iphunzitsa ciani makolo?

Yakobo 1.5

8. Kodi ndime iyi iuza ciani makolo amene abvutika pa kulera ana ao?
9. Kodi tingalekerere ana athu kupitiriza zoipa kulingana ndi ndime iyi?

- Kambiranani pamodzi mayankho. Mayankho abwino ali conco:

  Aefeso 4.25-32

  1. **Werenganinso ndime ya 25. Kodi makolo ayenera kucita ciani kulingana ndi ndime iyi?**
     Yankho: Ayenera kukamba coonadi nthawi zonse.
  2. **Kodi tiloledwa kukalipa?**
     Yankho: Inde, koma m'njira yabwino (modziletsa) ndipo tiyenera kuthetsa bvuto dzuwa lisanalowe. Zina za kulangiza zidzakambidwa m'phunziro 6.
  3. **Kodi mudziwa makolo amene anena zoipa (ndime ya 31)?**
     Yankho: Aloleni kuyankha pa yekha, mwacitsanzo kunyozetsa mwana mwa kumucha maina oipa, kupangira mwana coipa, kukakamiza ana kucita zoipa ndi zoletsedwa ndi Mulungu.
  4. **Werengani ndime ya 32. Citanthauzanji kukhala okoma wina ndi mnzace?**
     Yankho: Citanthauza kukhala ndi mtima wokoma ndi makhalidwe odzicepetsa. Kukhululukirana, kukhala m'mgwirizano.

  1 Atesalonika 5.15

  5. **Kodi tiyenera kucita ciani kulingana ndi ndime iyi?**
     Yankho: Tiyenera kucita zabwino.
  6. **Kodi kutsatira cokoma kutanthauza ciani?**
     Yankho: Kucita zimene ziri bwino pa maso pa Mulungu (cifukwa cace: ngati sitidziwa Baibulo lathu tidzalephera kutsatira cokoma): kukhala okoma mtima, ofuna kukhululukira, kulakalaka ciyanjano, kukhala monga Mulungu (cifukwa cace tiyenera kuyanjanitsidwa ndi Mulungu mwa Yesu kuti tionetse m'mene Mulungu aliri).
  7. **Kodi ndime iyi iphunzitsa ciani makolo?**
     Yankho: Kukhala acifundo, okoma mtima ndi ofuna kukhululukira. Ngati mufuna ana anu kukhala abwino, khalani citsanzo cao cabwino.

  Yakobo 1.5

  8. **Kodi ndime iyi iuza ciani makolo amene abvutika pa kulera ana ao?**
     Yankho: Kupempha Mulungu thandizo lake ndi kulowerera kwake.
  9. **Kodi tingalekerere ana athu kupitiriza zoipa kulingana ndi ndime iyi?**
     Yankho: Iai, tiyenera kupitiriza kuyesa mpaka iwo afika pa msinkhu wao. Koma angakhale kufika pa msinkhu wao, tikhoza kuwapempherera. Tiyenera kuwaonetsa cikondi cokhala ngati ca Kristu: kuwakonda monga Kristu akonda ana ake.

## 5. Zolowapo (15 minutes)

- Werengereni aphunzi zolowapo izi ndipo yankhani pamodzi mafunso.

  1. **Charles ndi Matilda**
     Charles ndi Matilda ali ndi ana awiri. Mwana m'modzi ali ndi zaka zisanu ndi ziwiri, wina ali ndi zaka zitatu. Charles ndi Matilda abvutika pa kulera ana ao, pakuti ana samvera nthawi zambiri. Charles akamba kuti, 'Pamene ndiwauza kupereka cinthu kwa agogo ao, iwo akana. Koma ngati ndiwauza kuti agogo adzawapatsa masweetie, iwo apita. Cifukwa cake ndimawauza tero. Pamene iwo afika nyumba ya agogo ao, sadzapeza masweetie, koma palibe bvuto, pakuti ndingofuna kuti andimvera.
     **Kodi munganene ciani kwa Charles ndi Matilda?**
     Yankho: Ayenera kukamba coonadi. Ndi cobvuta ndithu kuti ana samvera. Koma Mulungu afuna ife kulankhula coonadi nthawi zonse. Pemphani Mulungu nzeru kudziwa njira ya kulankhula coonadi. Phunzitsani ana anu, fotokozani bwino ndi momvetsa zimene iwo ayenera kucita. Khalani oima nji ndipo osasinthasintha pa m'mene muthana nao.

2. **Miriam**

   Miriam ali kholo losakwatiwa. Ali ndi ana asanu. Abvutika pa kuwalera. Alibe ndalama kuti iwo angaphunzire ku sukulu ndipo nthawi zambiri kulibe cakudya cowadyetsera. Miriam sadziwa cimene angacite. Tsiku lina mphwake wa ku Lusaka amutumira lamya. Samudziwa bwino, koma akambirana bwino. Potsiriza Miriam auza kuti alephera kudyetsa ana ao. Mphwake anena kuti afuna mtsikana kumthandiza pa nyumba ndiye angasamalire m'modzi wa ana akazi a Miriam.

   **Kulingana ndi inu, ndi ciani cimene Miriam adzaganiza za ici? Kodi mungacite ciani ngati ndinu Miriam?**

   Yankho: Lolani aphunzi kupereka mayankho ao. Malizitsani pa kunena kuti Miriam ali ndi ulamuliro pa mwana wake, ngakhale mwanayo akhala pa nyumba ya munthu wina.

   Zimene Miriam ayenera kucita: kupempha Mulungu thandizo (kumbukirani: Miriam ali ndi udindo woyamba wa pa mwana wake), kufufuza mbiri ya mphwake, kumfunsa mphwake kutuma ndalama kuti Miriam apitirize kusamalira mwana wake mogwiritsa nchito ndalama ya mphwake.

## 6. Kutsiriza (5 minutes)

- Bwerezani mwacidule zimene zaphunzitsidwa lero: makolo ndiwo zitsanzo za ana ao ndi za ana a m'mudzi. Ici ndi udindo waukulu. Khalani citsanzo cimene Mulungu afuna kuti muliri.
- Pempherani.

## Phunziro 6 Makolo Acikristu monga aziphunzitsi

Zofunikira pa nthawi ya kuphunzira
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

## 1. Kulandiridwa (5 minutes)
- Landirani onse.
- Pempherani.
- Bwerezani mwacidule zimene zinaphunzitsidwa m'maphunziro apitao: ukwati utanthauza ciyanjano. Mwamuna ayenera kutumikira banja lake mwa kuimirira m'malo mwa Mulungu. Mkazi ayenera kuthandiza mwamuna wake m'kuitanidwa kwake kwa kutumikira banja. Makolo ali ndi udindo wa kuphunzitsa ana ao. Awaphunzitsa mwa kukhala zitsanzo. Lero tidzaganizira njira ina ya kuphunzitsa: za zimene tinena kwa ana athu ndi za njira m'mene tilankhula nao.

## 2. Colinga ca kuphunzitsa ana – colowapo (10 minutes)
- Werengerani aphunzi colowapo ici ndipo afunseni ncifukwa ciani kuphunzitsa ana ndi kofunikira.
  *Dorothy ali ndi zaka makumi anai. Akamba kuti, 'Mai wanga sanali wokwatiwa pamene anali ndi mimba. Sindinadziwe konse tate wanga. Mai wanga anamwalira pa kubadwa kwanga. Umoyo wanga wonse ndinakhala pa nyumba ya mai wanga wamng'ono. Koma sanandisamalire. Anandipatsa cakudya ndi zobvala cabe. Sindinakhale m'modzi wa banja lao ndipo anandikana. Ndinangocita zimene ndinafuna. Ku sukulu ndinalibe anzanga, pakuti sindinali wokoma mtima ndipo ndinkaba. Mai wanga wamng'ono sanandiphunzitse. Cifukwa cace, pamene ndinakula sindinadziwe kuphika. Sindinakwatiwe konse pakuti anthu ananena kuti ndine munthu woipa.*
  Yankho: Kuphunzitsa ana ndi kofunikira, pakuti:
  1. Mulungu atiuza kucita tero. Ana ali ndi mitima yocimwa, cimodzimodzi monga anthu akulu. Makhalidwe ao ndi kucita zoipa. Cifukwa cace ayenera kuphunzitsidwa zabwino.
  2. Kopanda kuphunzitsidwa iwo sakhoza kukhala bwino mugulu la anthu ndipo adzakhala anthu osawerengedwa ndi osakwanitsa.

## 3. Mfundo za kuphunzitsa ana ndi kaphunzitsidwe kake – Kuwerenga Baibulo (30 minutes)
- Werengani pamodzi Miyambi 22.6 ndipo yankhani funso iri:
  1. **Cifukwa ciani mwana ayenera kuphunzitsidwa angakhale ali wamng'ono?**
     Yankho: Pakuti ana aphunzira msanga pamene ali ang'ono ndipo uphunzitsi udzawaletsa kucita zolakwa m'miyoyo yao.

- Werengani pamodzi Akolose 3.20, Aefeso 6.2 ndi Miyambi 6.20 ndipo yankhani mafunso awa
  2. **Kodi makolo ayenera kuphunzitsa ciani ana ao kulingana ndi ndime izi?**
     Yankho: Kukhala omvera.

- Werengani pamodzi Ahebri 12.10 ndi 11, Aefeso 6.4 ndi Akolose 3.21 ndipo yankhani pamodzi mafunso awa:
  3. **Kodi ndime izi zitiphunzitsa ciani za njira ya kulangiza ana?**
     Yankho: Kulangiza ana kuyenera kucitidwa mwa cikondi, kuphunzitsa zabwino, kukonza makhalidwe a mwana (osati kumcititsa mantha kapena kumkalipitsa kapena kumuonetsa kuti wamphamvu koposa ndi yani), kumvetsetsetsa mwana kuti walakwa ndiponso kuti ayenera kukhululukidwa ndi Mulungu. Dziwani kuti kulangiza si kumenya cabe: kulangiza kutanthauza kuphunzitsa, kukonza ndi kutsogolera mwana.

4. **Kodi njira zabwino za kulangiza ana ndizo ciani?**
   Yankho, mwacitsanzo:
   - Kuphunzitsa za m'Baibulo zifukwa za kuletsa makhalidwe ena ndiponso za zotsatira za makhalidwe otero.
   - Osaphweteka mwana m'thupi (kumkanira cakudya, mikwingwirima) kapena m'zokhudza (ganizirani mau anu) koma aphunzitseni. Zilango zina ziri ndi zoturukamo zina zosiyana ndi zimene mufuna (mwacitsanzo, kumenya mwana angampangitsa kukhala owukira kwa inu). Simufuna ana kucita mantha cifukwa ca inu, koma mufuna kukhala pafupi nao kuti mungakhudze mitima yao.
   - Osalangiza mwa kukalipa. Pempherani musanalange. Mukalephera kudziletsa, pemphani cikhululukiro ndipo yanjananinso.
   - Acitireni ana anu onse cimodzimodzi. Osalanga iwo osalakwa.
   - Mutalanga yanjananinso, khalani odekha mtima (Mulungu aleza mtima ndi ife, onetsani cifundo ndi cikondi cace!)

- Werengani pamodzi Salimo 119.9 ndipo yankhani funso iri:

5. **Kodi makolo acikristu ayenera kucita ciani?**
   Yankho: Kuphunzitsa ana ao za Mulungu. Ayenera kuphunzitsa Baibulo.
6. **Cifukwa ciani ana ayenera kuphunzitsidwa kulingana ndi Salimo 119.9?**
   Yankho: Cifukwa kopanda uphunzitsi iwo sangakhale ndi umoyo woyera.

- Werengani Afilipi 4.8 ndipo yankhani funso iri:

7. **Kodi ndime iyi itiphunzitsa ciani za zimene tiyenera kuphunzitsa ana athu?**
   Yankho: Tiyenera kukhala ozindikira zimene tiphunzitsa ndipo uphunzitsi wathu suyenera kutsutsana ndi Baibulo.

## 4. Umoyo wa masiku onse – miyambo (20 minutes)

- Fotokozani kuti zonse zimene ticita ndi kuphunzitsa ziyenera kulingana ndi cifuniro ca Mulungu. M'cikhalidwe ciriconse ca pa dziko muli mbali zimene zitsutsana ndi Baibulo.
- Funsani aphunzi za miyambo imene itsutsana ndi Baibulo.
  Yankho: Aloleni kupereka mayankho osiyanasiyana. Ngati alephera kuyankha, afunseni za miyambo ya ana akhanda, ya amuna ndi akazi amasiye, ya atsikana, ya iwo amene akonzekera ukwati ndipo afunseni zimene zimacitika pa nthawi ya matenda ndiponso pa maliro. Baibulo liyenera kukhala mtsogoleri wathu: dalirani pa Mulungu yekha, osapatsa malo kwa mizimu ndi miyambo kuikondweretsa mizimu, osakhala maliseche ndi zina zotere.
  Mulungu akamba kuti, 'Zinthu ziri zonse zoona, ziri zonse zolemekezeka, ziri zonse zolungama, zirizonse zoyera, ziri zonse zokongola, ziri zonse zimveka zokoma; ngati kuli cokoma mtima cina, kapena citamando cina, zilingirireni izi' (Afilipi 4.8). Osati cinthu cina, koma khalani oima nji ndipo dziwani kuti Mulungu athandiza iwo ofuna kucita cifuniro cace!

## 5. Zolowapo (30 minutes)

- Gawani gulu m'magulu atatu ndipo uzani gulu lirionse kukambira colowapo cimodzi.

1. **Aliyoni ndi Precious**
   Aliyoni ndi Precious ali ndi ana akazi anai ndi mwana wa mwamuna m'modzi. Mwana wao wamkazi woyamba ndi Lauzi. Lauzi ali ndi zaka 14. Anzake anakhala kale m'ndola. Precious anakana mpaka tsopano. Sadziwa ngati afuna mwana wake wa mkazi kukhala m'ndola. Ici cibvutitsa banja lonse, pakuti mbale wa Precious akamba kuti Lauzi sadzakwatiwa ngati sadzaphunzitsidwa bwino.
   **Funso: Kodi munganene ciani kwa Aliyoni ndi Precious?**

2. **Silvano and Mailesi**
   Silvano ndi Mailesi ali ndi ana asanu ndi m'modzi. Iwo adandaula cifukwa ca ana awo. Akamba kuti, 'Ana athu satimvera. Tiyenera kuwalanga masiku onse. Tiwamenya ndipo sitiwapatsa cakudya. Koma iwo sasintha. Komabe, cioneka monga atida ndiponso kuti angopitiriza kucita zimene afuna'.
   **Funso: Kodi munganene ciani kwa Silvano ndi Mailesi?**

3. **Avelina**
   Mwamuna wa Avelina anamwalira caka catha. Tsono Avelina ndi mkazi wa masiye ndiponso mai wa ana anai. Avelina anena, 'Kucokera pa nthawi ya kumwalira kwa mwamuna wanga, ine ndikumva kuti ndiri nekha ndiponso ndikumva cisoni. Ndiribe mphamvu kulera ana anga. Mwamuna wanga anali kuwaphunzitsa pamene iwo analakwa. Sindidziwa kucita ciani, ndiye ndingowalola kucita zimene afuna'.
   **Funso: Kodi munganene ciani kwa Avelina?**

- Itakomana 10 minutes, lolani magulu kupereka mayankho ao kwa gulu lonse.
  1. **Aliyoni ndi Precious**
     Yankho: Kumbukirani kuti tiyenera kucita zokondweretsa Mulungu. Aliyoni ndi Precious ndiwo otenga ulamuliro pa zimene mwana wa mkazi wao aphunzitsidwa. Mulungu afuna ife kukhala oyera ndi opanda zoipa pa maso pake. Aloleni kukambirana: Kodi miyambo ya atsikana ndi anyamata anamwali ilingana ndi Baibulo? Yankho: Iai! Akumbutseni za m'mene Mulungu afuna mwamuna ndi mkazi kukhala (maphunziro apitao): nthawi zambiri izi si zimene zaphunzitisdwa mwa miyambo. Cinthu cabwino koposa cimene Aliyoni ndi Precious angacite ndico kuphunzitsa mwana wao kulingana ndi Baibulo.
  2. **Silvano ndi Mailesi**
     Yankho: Khalani ozindikira pa njira m'mene muphunzitsa ana anu. Cioneka monga ana sanaphunzitse moyenera. M'malo mwa kulanga cabe, iwo makolo ayenera kuwauza zimene afuna kucita ndiponso kukhala citanzo cabwino. Atalanga ayenera kuyanjananso pakuti mwa njira ina ana adzamva mantha ndipo adzathawa.
  3. **Avelina**
     Yankho: Ana awafuna. Avelina angalemekeze mwamuna wake mwa kusamalira ana. Ayenera kukhala olimbika ndi kufunsa a m'banja, anzao kapena mamembala a mpingo kuthandiza pa njira ya kusamalira ana. Ngati saphunzitsa ana ao, iye adzakhala ndi mabvuto oculukirapo m'tsogolo.

## 6. Kutsiriza (5 minutes)

- Bwerezani mwacidule zimene zaphunzitsidwa lero. Ana ayenera kuphunzitsidwa za m'Baibulo cabe. Makolo ali ndi udindo pa kuphunzitsa zimene ziri zoyenera pa maso pa Mulungu ndiponso pa kutsogolera ana ao.
- Pempherani.

## Phunziro 7 Mabanja acikristu

Zofunikira za pa nthawi ya kuphunzira
- Baibulo
- Bolodi
- Coko

# 1. Kulandiridwa (5 minutes)
- Landirani onse.
- Pempherani.
- Bwerezani mwacidule zimene zinaphunzitsidwa m'maphunziro apitao.

# 2. Cikristu kunyumba – Kuwerenga Baibulo (40 minutes)
- Funsani aphunzi citanthauzo ca kukhala banja lacikristu: banjalo lioneka bwanji? Yankho: Werengani pamodzi ndime izi za m'Baibulo kupeza yankho.
- Werengani pamodzi Macitidwe a Atumwi 18.1-3 ndipo yankhani mafunso awa:
  1. **Kodi Paulo anapeza yani ku Korinto?**
     Yankho: Akula ndi mkazi wake Priskila.
  2. **Kodi tingadziwe bwanji kuti banja ilo linali banja lacikristu?**
     Yankho: Iwo analandira Paulo mtumiki wa Mulungu ndipo anali oceleza.
  3. **Kodi tingaphunzire ciani za Akula ndi Priskila kuli nchito?**
     Yankho: Banja liyenera kugwira nchito pamodzi.

- Werengani pamodzi Deuteronomo 6.4-8 ndi 20-25 ndipo yankhani mafunso awa:
  4. **Ndi yani amene atiuza kuphunzitsa ana athu?**
     Yankho: Mulungu.
  5. **Kodi tiyenera kuphunzitsa ciani ana athu?**
     Yankho: Za m'mene Mulungu aliri ndi za zimene Iye anacita.
  6. **Kodi tiyenera kuphunzitsa kuti ana athu?**
     Yankho: Paliponse.

- Werengani pamodzi Salimo 78.1-8 ndipo yankhani mafunso awa:
  7. **Kodi colinga ca kuphunzitsa ana za Mulungu ndico ciani?**
     Yankho: Kuti aike ciyembekezo cao kwa Mulungu ndiponso kuti kuphunzitse ana ao (ndime za 6 ndi 7).
  8. **Cifukwa ciani ndi cofunikira kuti ana aika ciyembekezo cao kwa Mulungu?**
     Yankho: Pakuti Mulungu yekha mwa Yesu akhoza kutipulumutsa ku macimo athu ndi kutibweretsa m'ubale wabwino ndi Iye. Mwa Yesu cabe tikhoza kukhala ndi moyo wabwino.
  9. **Kodi uphunzitsi wapamwamba wa m'Baibulo umene uyenera kuphunzitsidwa ndiwo ciani?**
     Yankho: Kulapa macimo (kumva cisoni ndi kuleka) ndi kukhulupirira Yesu monga Mpulumutsi weniweni (kudalira pa cipulumutso cace). Fotokozani mwacidule Yohane 3.16:
     - Kucokera ku nthawi yakuti Adamu ndi Hava sanamvere Mulungu, dziko lapansi ndilo dziko locimwa. Anthu ndiwo ocimwa; olekanitsidwa ndi Mulungu. Mulungu sanasinthike ndipo Iye ndi wacifundo: akondabe dziko lapansi.
     - Mulungu anatuma Yesu Kristu Mwana wake pa dziko lapansi kuti amwalire pa mtanda kukhululukira macimo. Kotero kuti anthu ocimwa akhoza kuyanjanitsidwa ndi Mulungu.
     - Aliyense amene adalira pa Yesu yekha pa cipulumutso, ndiye wopulumutsidwa ndithu. Cipulumutso ndico mphatso ya Mulungu mwa cisomo. Ndi mphatso yodabwitsa ndi yacilendo! Mulungu afuna anthu kulapa (kumva cisoni, kuleka macimo, kupempha Mulungu cikhululukiro) ndi kuika ciyembekezo cao mwa Iye yekha.

- Anthu a Mulungu ali ndi mtendere ndi Iye ndipo adzakhala naye Kumwamba muyayaya. Anthu ena onse alibe mtendere ndipo adzakhala ku Gehena muyayaya.

- Werengani pamodzi Mateyu 19.13-15 ndipo yankhani pamodzi funso iri:
  **10. Kodi makolo angapereke bwanji ana ao kwa Yesu?**
  Yankho: Mwa pemphero ndi kuwaphunzitsa za Yesu ndi cipulumutso cake.

- Werengani pamodzi Yoswa 24.15 ndipo yankhani pamodzi mafusno awa:
  **11. Kodi Yoswa ndi banja lake ananena ciani kwa anthu amene anapembedza milungu ina?**
  Yankho: M'ciriconse cimene cingacitike, iye ndi banja lake adzatumikira ndi kumvera Mulungu woona.
  **12. Kodi tingakhale bwanji oima nji m'kukana zonse zimene Mulungu aletsa?**
  Yankho: Tiyenera kukhala okhazikika mwa Mulungu. Mulungu ayenera kukhala Mutu wa banja lathu. Khalani olimba, werengani Baibulo kudziwa m'mene anthu a m'Baibulo anakhala ndipo pemphani Mulungu thandizo lake.

## 3. Umoyo wa banja lacikristu (20 minutes)

- Lembani mtengo waukulu pa bolodi.
- Funsani aphunzi za m'mene umoyo wa banja lacikristu uoneka. Kodi iwo acita ciani? Kodi makhalidwe ao ndi otani? Lembani mayankho ao abwino m'mtengowo.
  Yankho: Mwacitsanzo cikondi, ciyanjano, cikhululukiro, thandizo, uphunzitsi, ulemu, cipembedzo ca pa nyumba.
- Banja lacikristu ndilo monga mtengo wakubala zipatso zabwino zimene mamembala a m'banja (makamaka ana) ndi anthu ena angakondwere nazo: ubwenzi wabwino wa Mulungu mwa Yesu, ciyanjano, nzeru ndi zina zotere. Banja lacikristu ndilo kuunika m'mdima. Ici citanthauza kuti banja lacikristu libweretsa cisangalalo ndi cimwemwe m'dziko lodzala ndi mabvuto cifukwa ca macimo athu. Iwo athandizana ndi kuthandiza ena kuti ubwenzi wa Mulungu ndi anthu ena utukuke.
- Funsani aphunzi za m'mene banja lacikristu lionetsa ciyanjano cao ndi cikondi cao ca kwa Mulungu ndi ca anthu ena.
  Yankho:
  - Cipembedzo ca pa nyumba, mwacitsanzo kupemphera pamodzi, kupemphererana, kuwerenga Baibulo pamodzi kapena kuuzana nthano za m'Baibulu, kuimba, kutanthauzira Baibulo m'umoyo wa masiku onse. Mutu a nyumba uli ndi udindo wa kutsogolera cipembedzo ca pa nyumba.
  - Kupita ku calichi pamodzi: calichi ndi ya ananso. Athandizeni kukhala zii ndi kumvera! Kambiranani zimene zalalikidwa. Tsimikizirani kuti onse azimvetsa.
  - Khalani pamodzi nthawi ndi nthawi, mwacitsanso idyani pamodzi ndipo gwirani nchito pamodzi.
  - Pangani maganizo pamodzi. Mvererani ndipo ganiziranani maganizo. Ngati mwamuna ndi mkazi sabvomerezana, mkazi ayenera kudzigonjera.
  - Tandizani anthu ena. Makamaka iwo obvutika.
- Malizitsani pa kunena kuti ngakhale m'banja lacikristu zolakwika zipezekamo pakuti ife tonse ticimwa. Banja lacikristu ndilo banja lopatikiza ndi Kristu ndiponso banja limene lifuna kumkondweretsa Kristu. Osayesa kukhala umoyo wacikristu kopanda Kristu, cifukwa ici si cotheka.

## 4. Mayeso – osakakamiza (30 minutes)

- Kulemba mayeso ndi kosakakamiza. Ngati mufuna aphunzi kulemba mayeso, tengerani mayeso amene apezeka pa tsamba lotsiriza la buku liri musanayambe kuphunzitsa kapena awerengereni mafunso kapena lembani mafunso pa bolodi.
- Aloleni aphunzi kulemba mayeso.
- Congani mayeso. Mayankho abwino ali conco:

| | | | | | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| 1A | 2C | 3A | 4B | 5C | 6A | 7C | 8A | 9A | 10B |

## 5. Kutsiriza (5 minutes)

- Yamikirani aphunzi pa kubwera ku maphunziro.
- Alimbikitseni aphunzi kucita zimene anaphunzira. Osayesa kuzicita m'mphamvu yanu, koma pemphani Mulungu thandizo lake ndi kukhala umoyo wanu monga mwa cifuniro cace. Iye ndi wacifundo. Khalani olimbika!
- Pempherani.

# Mayeso Mabanja Acikristu

Stephanos

Dzina:……………………………………………

1. **Ndi ciani cimene ciri coona?**
   a. Ukwati ndiwo mphatso yocokera kwa Mulungu ndipo Mulungu ayenera kukhala maziko.
   b. Colinga ca miyoyo cathu ndico ukwati

2. **Cifukwa ciani muli mabvuto ambiri m'ukwati?**
   a. Pakuti anthu amvera malangizo oipa
   b. Cifukwa ca Satana
   c. Pakuti Adamu ndi Hava anacimwa. Ubwenzi wonse ndi woonongeka ndipo ndife ocimwa.

3. **Kodi ukwati wacikristu uli wotani?**
   a. Mwamuna ndi mkazi amene atumikira Mulungu komanso wina ndi mnzace m'mgwirizano ndi ciyanjano
   b. Mwamuna ndi mkazi amene amapemphera asanadye cakudya
   c. Mwamuna ndi mkazi amene apempha mbusa kudalitsa ukwati wao

4. **Kodi mwamuna wabwino amacita ciani, kulingana ndi Baibulo?**
   a. Mwamuna wabwino anyoza ndi kuuza mkazi wake kuti ali pansi, pakuti mwamuna ndi mutu wa nyumba
   b. Mwamuna wabwino akonda mkazi wake ndiponso ateteza ndi kusamalira banja
   c. Mwamuna wabwino adziganizira cabe ndipo ali waulesi

5. **Kodi mkazi wabwino amacita ciani, kulingana ndi Baibulo?**
   a. Mkazi wabwino amaoneka bwino kwambiri
   b. Mkazi wabwino angayende ndi mwamuna wina m'tseri
   c. Mkazi wabwino athandiza mwamuna wake kutumikira banja

6. **Ndi ciani cimene ciri <u>coona</u>?**
   a. Ana aphunzira zambiri za kuyang'ana makhalidwe athu kuposa kumvera mau athu
   b. Ana si ofunikira m'maso mwa Mulungu
   c. Colinga ca kukhala ndi ana ndico kuti angatisamalire pamene ndife okalamba

7. **Ndi ciani cimene ciri <u>bodza</u>?**
   a. Mulungu atiuza kuphunzitsa ana athu kumvera Mulungu ndi kumlemekeza
   b. Kopanda kuphunzitsidwa, ana sakhoza kukhala bwino m'mugulu la anthu
   c. Ndi cabwino kuphunzitsa ana maphunziro a miyambo a cikhalidwe amene atsutsa ndi Baibulo

8. **Kodi cofunikira pa nthawi ya kulanga mwana ndico ciani?**
   a. Kufotokoza, kudzudzula makhalidwe oipa ndi kuphunzitsa makhalidwe abwino
   b. Kumenya kwambiri
   c. Kunyoza mwana ndi kumcititsa mantha

9. **Kodi cofunikira ndico ciani m'banja lacikristu?**
   a. Kupembedza Mulungu pamodzi, kukhala pamodzi nthawi ndi nthawi, kukondana, kuthandiza anthu ena
   b. Kugwira nchito molimba
   c. Kutuma ana ku sukulu

10. **Kodi uphunzitsi wapamwamba wa m'Baibulo umene uyenera kuphunzitsidwa kwa ana ndiwo ciani?**
    a. Ngati timvera Mulungu, tidzakhala olemera
    b. Ife anthu ocimwa tiyenera kuyanjanitisidwa ndi Mulungu mwa Yesu Mpulumutsi
    c. Aliyense amene amapemphera ndi kupita ku calichi adzapita Kumwamba

11. **Chulani zinthu ziwiri zimene munaphunzira za ukwati wacikristu ndi mabanja acikristu.**

    1. ……………………………………………………………………………………………………………

       ……………………………………………………………………………………………………………

    2. ……………………………………………………………………………………………………………

       ……………………………………………………………………………………………………………